## A CIGAWO COYAMBA – CIMANGIRIZO [MAKISI 40]

**Lemba cimangirizo m'Cinyanja comveka bwino pa mutu umodzi wa mitu yotsatirayi. Cimangirizo cako cikhale pakati pa mau 250 ndi 350.**

**Mitu ya nkhani.**

1. Tiyerekeze kuti iwe ndi abale ako munapita kukacitira cuti ku nkhalango (National Park) ina yake. Fotokoza mwatsatane-tsatane za malowo.
2. Makono kwadza mliri wochedwa 'Corona'. Lemba mwatsane-tsatane m'mene mliri umeneyu wasautsira anthu.
3. Fotokoza za kukoma ndi kuipa kwa aphunzi amuna ndi akazi kuphunzirira pa modzi.
4. Tayerekezera kuti pa maphunziro ako unali kulipiridwira ndalama za sukulu ndi munthu wina wake amene sali wa cibale. Tsopano wamaliza sukulu lako. Lemba kalata kwa munthuyo kumthokodza pa zomwe anakucitira.

## B CIGAWO CACIWIRI – ZA M'MABUKU [MAKISI 40]

**Yankhani molunjika mafunso ya m'mabuku anai cabe mwa asanu awa.**

**1 MATSTOTSI** *(G.H. Shonga ndi J. N. Zulu)* **[Makisi 10]** www.eczpastpapers.com

(a) Kodi liu lakuti 'tsotsi' litanthauzanji? [2]

(b) Nanga Gonaapa Mazani anali ndani m'bukuli? [1]

(c) Chula dzina la mkazi yemwe mwamuna wake anaphedwera mnyumba ndi matsotsi. [1]

(d) Pereka milandu iwiri cabe imene anamangidwira nayo Efa. [2]

(e) M'bukuli muli mwambi wakuti, "mtsipu wobiriwira unapha mbuzi." Masulira mwambiyu kulingana ndi m'mene zinaliri m'bukuli. [4]

**2 MASAUTSO A KAM'NJIRA** *(J. N. Banda)* **[Makisi 10]**

(a) Timvetsanji tikati, "Masautso?" [1]

(b) Fotokoza mwatsatane-tsatane m'mene Kamnjira anadzipezera mkamsakasa. [4]

(c) Chulani dzina la mkazi amene Kamnjira anakwatira. [1]

(d) Pereka umboni uwiri umene utisimikizira kuti azungu a mishoni anadzadi kudzaombola anthu mu ukapolo. [4]

 www.eczpastpapers.com 

**3 CIKONDI SAUMIRIZA** *(J. N. Banda)* **[Makisi 10]**

(a) Perekani zitsanzo ziwiri zimene zisonyeza kuti Chale anali kuumiriza cikondi. [2]

(b) M'bukuli muli mau akuti, "Ndiri bwino pang'ono koma citani condimwetsa."

(i) Ndani ananena mauwa? [1]

(ii) Anali kuuza yani. [1]

(iii) Fotokozani mwatsatane-tsatane zimene zinamcitikira munthuyu kuti alankhule mauwa. [4]

(c) M'bukuli muli mau akuti, 'Amai a Liza.'

(i) Ndani analankhula mauwa? [1]

(ii) Chula dzina la munthu wina amene analipo pa nthawi yolankhulidwira mauwa ku cotserako wolankhula ndi woyitanidwayo. [1]

**4 IKAKUONA LITSIRO – SIKATA** *(J. M. Ntaba)* **[Makisi 10]**

(a) Chula zifukwa ziwiri zimene munthu angamangidwire kulingana ndi bukuli. [2]

www.eczpastpapers.com

(b) Umvetsanji tikati, "mbiri ndi ng'oma?" [2]

(c) N'cifukwa ciyani Bonondo anabvulira nsapato pamene anali kuponda pa mcenga wa kunyanja? [2]

(d) Kodi basi linadzaliranji mopitirira pa muyeso? [2]

(e) Chula mitundu iwiri ya nthoci imene inachulidwa m'bukuli. [2]

**5 MALIRO NDI MIYAMBO YA ACHEWA** – *(A. J. Makumbi)* **[Makisi 10]**

(a) Pereka matanthauzo ya malangizo awa kwa namwali.

(i) Mkazi amamva nkhwali. [2]

(ii) Mwamuna uzimupenya kumimba nkhope sisintha. [2]

(b) Fotokozani m'mene zinali kucitikira ngati mkazi wa kucitengwa wamwalira. [5]

(c) Kodi ndi cifukwa ciyani anthu ayenera kupitira kucipatala atadwala? [1]

www.eczpastpapers.com

C CIGAWO CACITATU – MIYAMBI NDI MIKULUWIKO [MAKISI 20]

**Uyenera kuyankha mafunso onse m'cigawo ici (1 ndi 2)**

**1 Miyambi [Makisi 10]**

**Pereka matanthauzo a miyambi yotsatirayi:**

**(a)** Maso aipsya kamwa likonza.

**Yankho:** ............................................................................................ [2]

**(b)** Ketengera zinthu pamgon'o.

**Yankho:** ............................................................................................ [2]

**(c)** Kudza kwa mafinya ndi munga womwe.

**Yankho:** ............................................................................................ [2]

**(d)** Kutemetsera nkhwangwa pamwala.

**Yankho:** ............................................................................................ [2]

**(e)** Kanthu kali munye/kanthu kali kucala.

**Yankho:** ............................................................................................ [2]

www.eczpastpapers.com

**2 Mikuluwiko [10]**

**Pereka matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi. Kenaka uigwiritsire nchito m'ziganizo za m'Cinyanja comveka bwino kusonyeza kuti ukuidziwadi.**

**Citsanzo:** Kanjipiti

**Tauthauzo:** Munthu wamfupi.

**Ciganizo:** Zimbani anakwatira Kanjipiti.

**(a)** Cimunthu:

**Tanthauzo:** ............................................................................................ [1]

**Ciganizo:** ............................................................................................ [1]

**(b)** Kadzioche:

**Tanthauzo:**............................................................................................ [1]

**Ciganizo:** ............................................................................................ [1]





www.eczpastpapers.com

**(c)** Khambi:

**Tanthauzo:**.................................................................................. [1]

**Ciganizo:** .................................................................................. [1]

**(d)** Matula:

**Tanthauzo:**.................................................................................. [1]

**Ciganizo:** .................................................................................. [1]

**(e)** Sisita:

**Tanthauzo:**.................................................................................. [1]

**Ciganizo:** .................................................................................. [1]

**Mayeso Anu Atha**

www.eczpastpapers.com



www.eczpastpapers.com